# KAMBILONJO FULL PRIMARY SCHOOL
## 2018 – 2019 SCHOOL YEAR
## STANDARD 7 END OF TERM I EXAMINATIONS
## CHICHEWA
(100 marks)

Dzina: ______________________________________________

Malangizo Nthawi: 2 hours

(i) Onetsetsani kuti tili ndi magawo anayi. Gawo A, B, C ndi D.
(ii) Lembani dzina lanu.

GAWO A (malikisi 30)

Yankhani funso limodzi la chimangirizo. Mawu a chimangirizo asachepere 100 komanso asabzole 150.

1. Lembani chimangirizo pa mutu uwu: UKHONDO
Mwa zina tsatani izi polemba:

Ndime yoyamba
- Zitsanzo zina za ukhondo.
- Kufunika kochita ukhondo m'makomo mwathu.

Ndime yachiwiri
- Ena mwa mavuto omwe amadza kaamba kosowa ukhondo m'makomo mwathu.
- Zina zomwe tingachite polimbikitsa anthu pa nkhani ya ukhondo.

Ndime yachitatu
- Zomwe Boma kapena mabungwe ena akuchita pofuna kulimbikitsa anthu pa nkhani ya ukhondo.

______________________________________________
______________________________________________
______________________________________________
______________________________________________
______________________________________________
______________________________________________
______________________________________________
______________________________________________
______________________________________________
______________________________________________
______________________________________________
______________________________________________
______________________________________________
______________________________________________
______________________________________________
______________________________________________
______________________________________________
______________________________________________
______________________________________________
______________________________________________
______________________________________________
______________________________________________
______________________________________________
______________________________________________

________________________________________________________________________________
________________________________________________________________________________
________________________________________________________________________________
________________________________________________________________________________
________________________________________________________________________________
________________________________________________________________________________
________________________________________________________________________________

GAWO B (malikisi 20)

2. Werengani nkhani yotsatirayi mosamala kwambiri kenaka yankhani mafunso otsatirawo

Kalekale m'dziko la Chipala mudali mfumu yotchedwa Mtupatupa yomwe idali yolemera kwambiri. Mfumuyi idali ndi ana awiri.Woyamba ankatchedwa Tepatepa ndipo wachiwiri adali Ganiza.

Mfumu Mtupatupa idali ndi zifuyo zochuluka monga: ng'ombe, mbuzi, nkhuku, abakha ndi nkhunda. Pakhomo pake padali pa mwana alirenji. Ponena mwatchutchutchu mfumuyi idali mpondamatiki.

Mwadzidzidzi mfumu Mtupatupa idadwala koopsa ndipo idayitanitsa ana ake aja kuti ikambe nawo. Iyo idapempha ana aja kuti aliyense anene zokhumba zake iyo idakali moyo.

Tepatepa adali wayamba kunena za khumbo lake lenileni Lomwe lidali lakuti atate ake achire. Choncho mfumu Mtupatupa idatenga ndodo ziwiri niyipereka imodzi kwa mwana aliyense. Iyo idawalimbikitsa anawo kuti aliyense akasungitsitse ndodo yake.

Madzulo atsikulo, Tepatepa adavutika mumtima. Adatenga ndodo ija nayithyola ndi kuyiponya pamoto. Iye adawadandaula atate ake chifukwa chomupatsa ndodo m'malo mwa chuma.

M'mawa kutacha mfumu Mtupatupa idayitanitsa nduna zake zonse, mikoko yogona, achibale, nkazi ndi ana ake. Iyo idauza gulu lonse kuti ikufuna kugawira chuma ana ake kuti asadzalimbane patsogolo.

Mfumuyi idauza mwana wake Tepatepa kuti atenge ndodo yake ndi kuloza chomwe akufuna. Apatu Tepatepa adangoti kakasi. Iye adayamba kulira nakalowa m'nyumba mwake.

Mfumu itamva zomwe Tepatepa adachita ndi ndodo yake ija idauza Ganiza mwana wake wina kuti akatenge ndodo yake ndi kuloza zomwe akufuna. Ganiza adatenga ndodo yake ndipo adaloza chuma chonse pamodzi ndi atate ake. Pa ichi mfumu Mtupatupa idauza mwana wake Ganiza kuti chuma chonse waloza chidzakhala chake komanso poti waloza iye mfumu, ufumunso udzakhala wake iyo ikadzamwalira. Anthu adawomba m'manja ndipo nthungululu zidamveka ponseponse.

Tsopano Yankhani mafunso otsatirawa.

a. Kodi mfumu Mtupatupa inkakhala kuti? (1 malikisi)

________________________________________________________________________________

b. N'chifukwa chiyani mfumu idayitanitsa ana ake? (2 malikisi)

________________________________________________________________________________

c. Tchulani zinthu ziwiri zotsimikiza kuti mfumu Mtupatupa idali yolemera.

(i)__________________________________________________________________________(1 malikisi)

(ii)_________________________________________________________________________(1 malikisi)

d. Kodi Tepatepa ndi Ganiza adalandira chiyani kuchokera kwa atate awo? (2 malikisi)

________________________________________________________________________________

e. N'chifukwa chiyani Tepatepa adakhala wovutika mumtima mwake? (2 malikisi)

________________________________________________________________________________

f. Fotokozani cholinga chenicheni cha mfumu Mtupatupa poyitanitsa gulu la anthu pamodzi ndi banja lake. (2 malikisi)

________________________________________________

g. Perekani matanthauzo a mawu otsatirawa:
(i) "mponda matiki" ________________________________(1 malikisi)
(ii) "adangoti kakasi" ________________________________(1 malikisi)

h. Pezani mawu m'nkhaniyi womwe ali ndi matanthauzo ofanana ndi awa:
(i) "ziweto" ________________________________(1 malikisi)
(ii) "akuluakale" ________________________________(1 malikisi)

i. N'chifukwa chiyani Tepatepa adalephera kulandira chuma kuchokera kwa atate ake? (2 malikisi)

________________________________________________

j. Tchulani zinthu ziwiri zomwe Ganiza adaloza. (2 malikisi)

________________________________________________

k. Pelekani mutu wa nkhani yomwe mwawerengayi? (2 malikisi)

________________________________________________

## GAWO C (malikisi 10)

Yankhani mafunso onse awiri m'gawoli.

3. Werengani kankhanika ndipo muyankhe mafunso otsatirawo.

A Khwasulani :Odi! Odi!

A Naphiri :Eee! Tikuopeni bambo. Nanga mwangotiyendera?

A Khwasulani :Musandiope kwambiri. Kaya amuna anu alipo?

A Naphiri :Ayi palibe. Momwe achokera m'mawa sanabwere.

A Khwasulani :Chabwino, ndachita mwayi sindivutika ndikuyenda popeza a Naphiri, a Namgambi ndi a Nakhwinda muli pompano. Mawa kuli liwamba. Nachi chimanga chofiira mudzapatse amuna anu.

A Naphiri : Zikomo kwambiri, mawa tidzatsuka m'kamwa.

MAFUNSO

(i) Kodi ndi malonje anji omwe mwawerengawa? (1 malikisi)

________________________________________________

(ii) Kodi malonjewa a Khwasulani ndi ndani? (1 malikisi)

________________________________________________

(iii) Tchulani njira imodzi yotumizira uthenga wa maliro kumudzi. (1 malikisi)

________________________________________________

(iv) Kodi mukamayankhula ndi akuluakulu mumayenera kutani? (1 malikisi)

________________________________________________

(v) Kodi m'mudzi mukagwa maliro uthenga woyamba umayenera kupita kwayani? (1 malikisi)

________________________________________________

4. Kupanga ziganizo
Pangani ziganizo zomveka bwino ndi mawu awa:

(i) "jejemera":________________________________(1 malikisi)
(ii) "msoti":________________________________(1 malikisi)
(iii) "mkwatibwi": ________________________________(1 malikisi)

(iv) "pansewu": ______________________________________________ (1 malikisi)

(v) "wanga" :______________________________________________ (1 malikisi)

GAWO D (malikisi 40)

Zungulizani lembo lokhoza (A, B, C kapena D) m'mafunso otsatirawa.

Mafunso 6 mpaka 9. Sankhani mitundu ya mawu omwe ali ndi mzere kunsi kwawo mziganizo zotsatirazi:

5. Mwana wanga sakonda kudya nsima.
   A. mlowam'malo C. mfotokozi
   B. dzina D. mneni
6. Amene sakufuna asiye.
   A. mneni C. mlumikizi
   B. mlowam'malo D. mvekero
7. Iwo adandilandira mwachikondi.
   A. muonjezi C. dzina
   B. mneni D. mfotokozi
8. A Dzonzi adzabwera m'kuja.
   A. mfotokozi C. muonjezi
   B. mneni D. dzina
9. Zanga zidatha dzulo.
   A. muonjezi C. dzina
   B. mlowam'malo D. mfotokozi

Mafunso 10 mpaka 14. Perekani matanthauzo a mikuluwiko yotsatirayi:

10. Pawiripawiri sipauzilika.
    A. kanthu nkavumbu
    B. kumachita zinthu zambiri nthawi imodzi umalephera zonse nthawi zina
    C. nsima ukapusa imakuwotcha
    D. osamachita zinthu mwachibwana
11. Walira mvula walira matope.
    A. pomwe pali zabwino umayenera kukumana ndi zovuta.
    B. kunja kukagwa mvula kumakhala matope
    C. kumachenjera pamalo
    D. umayenera kuvala jombo ndi kutenga sumbulera
12. Kukana nsalu ya akulu nkuviika.
    A. kuchita zinthu mwaulemu
    B. kulimba mtima zinthu zikachitika
    C. kugona pa udzu
    D. kuchita chinthu chifukwa cha mwamanyazi
13. Khoswe wapatsidwi adaulula wa padzala.
    A. kuchenjeletsa pamalo sibwino
    B. kufatsa kumathandiza kupewa zovuta
    C. zabwino zimatha kupezeka pa malo wobisika
    D. nkhani imatha kuulula inzake yobisika
14. Aonenji adapha mvuwu m'mono.
    A. kupalamula mlandu nkulinga uli ndi nkhuku
    B. munthu wonyozeka amatha kuchita zinthu zazikulu.
    C. kumachita zinthu modekha
    D. zonse ndi zolondola.

Mafunso 15 mpaka 19. Sankhani gulu la mayina a mawu omwe ali m'munsiwa:

15. katambala
    A. Mu-, Mi- C. Mu-, A-
    B. Li-, Ma- D. Ka-, Ti-
16. fuko
    A. I-, Zi- C. Chi-, Zi-
    B. Li-, Ma- D. U-, Ma-
17. munda
    A. Mu-, Mi- C. Chi-, Zi-
    B. Ka-, Ti- D. U-, Ma-
18. maukwati
    A. Mu-, A- C. U-, Ma-
    B. Mu-, Mi- D. Ka-, Ti-
19. kubwalo
    A. Mu-, A- C. U-, Ma-
    B. Mu-, Mi- D. Ku-, Pa-, Mu-

Mafunso 20 mpaka 24. Sankhani mawu otsutsana m'matanthauzo ndi otsatirawa:

20. nkhondo
    A. chimwemwe C. mtendere
    B. chisangalalo D. ulemerelo
21. tonde
    A. msoti C. msona
    B. thadzi D. mkota
22. kumpoto
    A. kuvuma C. kum'mawa
    B. kuzambwe D. kum'mwera
23. Mpongozi
    A. nkaziwako C. tatavyala
    B. nkamwini D. mwanako
24. Wang'ono
    A. wamkulu C. akuluakulu
    B. akulu D. wakulu

MAYESO ATHERA APA

(LINGUISTIC DEPARTMENT)